KATEMERA

Mtumiki wathu (SAW) adapereka malangizo otsatirawa kwa Ibn Abbaas (RA):
" Mteteze Allah(potsatira zolamura zake)ndipo Allah azakutetezanso,ndipo ndithu uteteze zomwe Allah wakulamura ndipo chithandizo cha Allah chizakhala nawe.Ndipo ukafuna kupempha pempha Kuchokera kwa Allah, ndinso ukafuna thandizo pempha thandizo Kuchokera Kwa Allah.Ndipo zindikira kuti anthu onse atasonkhana Kuti akuthandize thandizo,sangathe kukuthandiza kupatula chokhacho chomwe Allah adakhonza kale ndipo chidalembedwa kuti chikuchitikire,ndiponso ngakhale atasonkhana Kuti akupezese vuto sangakupezese vuto kupatula ngati Allah adakhonza ndipo zidalembedwa kale kuti vutolo lizakupeza,zolembera zolemba za zomwe zizakuchitikire pamoyo wako zidanyamulidwa kale m'mwamba ndipo inki pa mapepala idauma kale.
(Tirmidh 2516)

Kuchedwetsa ndi chisamalo ndi kochokera Kwa Allah ndipo kufulumizisa ndi kochokera kwa Satana (Tirmidh 2012).

Talandira mafunso ochuluka okhudzana ndi pologalamu ya katemera wa covid-19.

Koma pambuyo potenga nthawi kupanga kafukufuku komanso kuyang'anitsitsa ndinso kuphatikiza kukumana ndi akadaulo azaumoyo, ndipo Ife pa udindo komanso pa ntchito yathu tapeza zotsatira zikudzazi:

- Kupatula potengera malamuro a chipembedzo ,pakuyenera kutsindika kuonetsetsa zinthu zomwe zikupezeka mkati mwake polandira thandizo lililonse,poyang'ana chitetezo cha munthu,ndinso kuona ziopsezo zomwe zingaike moyo pa chiswe ,powononga umoyo wamunthu ndinso thanzi.
- Madandaulo okhudza katemera wa covid-19 pakupezeka zinthu zomwe zili zoika umoyo wamunthu pachiswe,zomwe zingabwerese matenda okhudzana ndi chitetezo cha mthupi, komanso katemerayu ndiyemwenso angapangitse matenda a covid-19 kufika povuta zedi kuposera momwe matendawa alili pambuyo potenga katemerayu.Ndipo pali nkhawa zomwe zikupezeka kuti zidaikidwa kale mmbuyomu za zovuta ndi zowawa zokhudza katemera wa covid-19 nde sizikuziwika kuti nkutheka mwina munthu yemwe angatenge katemera ameneyu wa covid-19 mwina nkukumana ndizovutazi komanso zopwetekazi.
  Powonjezera apo mmayiko ena zatipeza ndithu kuti chiwelengero cha anthu omwalira ndipomwe chikumakwera kwambiri pambuyo poti anthu abayidwa katemera ameneyu wa covid-19, ndiponso kuyezedwa koti katemera ameneyu ndi othandizadi sikudakhazikitsidwe.
- Popitilira apo, ndizomveka kwambiri kuti kugawa katemera ameneyu mmaiko osiyana siyana ndithu afulumizitsa kwambiri, zikutheka bwanji ntchito ndithu yomwe pachikhalidwe ingathe kutenga zaka zisanu kufikira khumi ndikuipanga m'miyenzi yowerengeka chabe.Mwachionekereni pasoweka njira ya chitetezo yapakati kati ngakhalenso yayitali yotulutsira katemera ameneyu.

Ngati asilamu pakufunika kuonetsetsa umoyo wathu,ndinso kuzitchinjiriza kuzonse zomwe zingaike umoyo wathu padiwa,ngati nthenda yatigwera tikuyenera kutsata njira yokhayo yomwe ndi yovomerezeka pa chipembedzo cha chisilamu, komanso tikuyenera kugwirisa michizo yokhayo yomwe tili nayo chikhulupiliro kuti ndiyothandiza komanso tikuyenera kupewa njira zonse zomwe tikuziwa ndi kuzikaikira kuti zingatibwerese mavuto pa umoyo wathu.
Potengera pa malamuro achipembedzo pankhani imeneyi Pali zokaikitsa zomwe zikupezeka mkati mwake, zomwe zikupezeka padakali pano ndizoti pali njira zopewera mululiwu osati mankhwala.Ndipo Ife sitikulimbikisa zotenga katemera ameneyu ndipo tikuchenjezani kuti mumutalikire ndipo musamale.

Mtumiki wathu okondedwa (SAW) adatiphunzisa Ife njira zomwe tingazitetezere kuzoipa komanso kumatenda osiyana siyana, ndipo tikulangizidwa kuwerenga duwa yotsatirayi kokwana katatu m'mawa komanso madzulo alionse;

اللّهُمَّ عَافِنِيْ فِيْ بَدَنِيْ، اللّهُمَّ عَافِنِيْ فِيْ سَمْعِيْ، اللّهُمَّ عَافِنِيْ فِيْ بَصَرِيْ، لَا إِلٰهَ إِلَّا أَنْتَ

Oh Allah ndipaseni ine chitetezo ndinso ubwino pathupi langa, oh Allah ndipaseni ine chitetezo ndinso ubwino mmakutu anga,oh Allah ndipaseni ine ubwino mmaso anga, ndithudi palibe Mulungu wina opembedzedwa kwa choonadi koma Allah inu nokha. (Abu Dawood)

Timpemphe Allah alisunge ndikuliteteza thanzi lathu komanso chikhulupiliro chathu,ndipo atipase umoyo wabwino muchipembedzo chathuchi ,pano padziko lapansi ngakhalenso Ku moyo uli nkudzawo
Ameen

MGWIRIZANO WA MAULAMAA KUNO KU SOUTH AFRICA

25 Jumād al-Ākhirah 1442 / 08 February 2021

WIFĀQUL 'ULAMA (SA)
ASSOCIATION OF SOUTH AFRICAN 'ULAMA

ASPIRING TO PRESERVE THE ESSENCE OF SUNNAH